Pewani Kulakalaka Zinthu Zoipa

Davide ndi Bati-seba—Gawo 1

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Mukamawerenga mavesiwo, mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula. Yesani kumva mmene anthu a mu nkhaniyi akumvera mu mtima mwawo.

Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi: Davide, Bati-seba, Uriya ndi Yoabu

Chidule cha nkhaniyi: Davide anachita tchimo lalikulu ndipo anayesetsa kuti alibise.

1 GANIZIRANI ZIMENE ZINACHITIKA.—WERENGANI 2 SAMUELI 11:1-27.

Jambulani chithunzi cha mmene inuyo mukuganizira chosonyeza mmene denga limene Davide anakwerapo pa nthawi imene anaona Bati-seba akusamba linkaonekera. Mungajambule pamene panali Davide komanso pamene panali Bati-seba.

Kodi mukuganiza kuti anthu otsatirawa, omwe atchulidwa kwambiri m'nkhaniyi, anali ndi makhalidwe otani?

Davide _____

Bati-seba _____

Uriya _____

Yoabu _____

Kodi mukuganiza kuti Uriya ankamva bwanji mumtima pamene ankalankhula ndi Davide, mawu omwe ali muvesi 11?

_____

_____

2 FUFUZANI MOZAMA.

Kodi mukuganiza kuti Yowabu anathandizira bwanji kuti Uriya aphedwe? (*Werenganinso vesi 14-17.*) _____

_____

Kodi mukuganiza kuti Bati-seba anali ndi mlandu uliwonse pa zimene zinachitikazo? (Zokuthandizani: *Werenganinso 2 Samueli 11:4;* kenako werengani Levitiko 20:10.) _____

_____

Kodi mukuganiza kuti Davide anafunika kukhala ali kuti pa nthawi imene ankaona Bati-seba? (*Werengani 2 Samueli 11:1.*) _____

_____

Baibulo linalosera kuti Mulungu adzaukitsa anthu ambirimbiri amene anamwalira. Kodi mukuganiza kuti zinthu zidzakhala bwanji Davide, Uriya, Bati-seba ndiponso Yowabu, akadzaukitsidwa n'kuyamba kufunsana kuti aliyense afotokoze zimene zinachitika zokhudza nkhaniyi? _____

_____

_____

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Kodi Davide anaphwanya malamulo ati, ndipo anayenera kupatsidwa chilango chotani? (Zokuthandizani: Werengani Ekisodo 20:13, 14, 17; komanso Genesis 9:6; Deuteronomo 22:22.) _____

_____

Kodi tingati Davide anaphwanya bwanji lamulo limene lili pa Ekisodo 20:15?

_____

_____

3 GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA.

Lembani zimene mwaphunzira zokhudza . . .

Kuopsa kopitiriza kulakalaka zinthu zoipa. (Yakobo 1:14, 15) _____

_____

Kuopsa kuchita zinthu zimene talamulidwa ngakhale kuti n'zotsutsana ndi malamulo a Mulungu. _____

_____

Zotsatirapo za tchimo, ngakhale tchimolo litakhala kuti silinaonekere kwa inuyo kapena kwa ena. (*Werenganinso 2 Samueli 11:27.*) _____

_____

4 DZIFUNSENI KUTI.

Kodi ndi pa nthawi kapena zochitika ziti pamene ndingayesedwe kuti ndizingoyang'anitsitsa zinthu zimene zingandichititse kuti ndizilakalaka zinthu zoipa?

_____

_____

Kodi ndingatani kuti ndisamalakelake zinthu zimene Mulungu amadana nazo? _____

_____

M'nkhaniyi, kodi ndi mfundo iti imene yandikhudza mtima kwambiri, ndipo n'chifukwa chiyani? _____

_____

Mungachite izi: Yerekezani kuti ndinu mtolankhani ndipo mukupereka lipoti la nkhaniyi pa wailesi kapena pa TV. Fotokozani zimene zinachitika ndipo mufunse mafunso anthu amene akutchulidwa m'nkhaniyi komanso amene anaona pamene zinthuzo zinkachitika.

JW.ORG™

Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania